# UNDUNA WA ZANYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO

## NTHAMBI YOONA ZANYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO


## ULOSI WA KAGWEDWE KA MVULA M'DZINJA LA 2025 - 2026, M'BOMA LA NKHATABAY

# DZINJA LA 2025 - 2026 MWACHIDULE

Katenthedwe ka Nyanja ya mchere ya Pacific sikakhudza kwambiri nyengo ya dzinja ya 2025/26.

Boma la Nkhatabay likuyembekezera kulandira mvula ya mlingo wokhadzikika kapena kuposerapo ngakhale pali kuthekera kwakukulu koti mvula yochepera mlingo wokhadzikika itha kudzagwa mu November 2025, komanso February 2026.


## October 2025




Nyengo yotentha ndi yopanda mvula ikuyembekezeka m'madera ochuluka m'boma la Nkhata bay mu October.


Pali kuthekera kolandira mvula ya chizimalupsya yosapitilira mlingo wa 50 mm m'madera ena a m'bomali .

## November 2025





Boma la Nkhata bay lizapitirira kukumana ndi nyengo yotentha komanso yopanda mvula mu November. Madela ena m'bomali angathe kulandira mvula yochepera mulingo wokhadzika. Pali kuthekera kwakukulu kokhala pa chiopsezo cha Mphenzi, Mphepo ya nkuntho ndi Mvula ya ziphaliwali.
Madera ena a mphepete mwa Nyanja ayembekezere kulandira mvula yapakati pa 50 mm ndi100 mm.

## December 2025





Madera ambiri m'bomali, ayembekezere kulandira mvula yoposera mlingo wokhazikika kapena kuposera apo wa pakati pa 150 mm ndi 200 mm.
Madera ena a mwa TA Kabunduli, TA Timbiri, Nkhatabay boma, SC Nyaluwanga komanso Usisya ayembekezere kulandira mvula yochepera mlingo wokhazikika mwezi umenewu.
Mvula yokhazikika m'boma la Nkhatabay ikuyembekezeka kugwa kuyambira sabata la chitatu la mwezi wa December 2025,

## January 2026




Madera ochuluka m'boma la Nkhata bay ayembekezere kulandira mvula y mlingo wokhadzikika kapena kuposera apo ya pakati pa 150 mm ndi 200 mm.
M'madera ena amwa SC Zilakoma komanso kumwera kwa TA Kabunduli mutha kudzagwa mvula ya mlingo wa pafupifupi 250 mm.
Pali kuthekera kwakulu koti m'madera ena m'bomali mutha kudzakhala ng'amba ya sabata imodzi mu January.


## February 2026




Bomali liyembekezere mvula ya mlingo wokhadzika kapena kuchepera apo yomwe ndi yapakati pa 150 ndi 200 mm.

Chiopsezo cha ng'amba ndi chocheperako mu February, 2026 ngakhale kuti madera ena m'bomali mutha kudzachitika ng'amba ya sabata imodzi.


## March 2026




Mwezi wa March boma la Nkhatabay liyembekezere kulandira mvula yochuluka.
Madera ambiri akumpoto kwa bomali ayembekezere kulandila mvula ya pakati pa 150 mm ndi 200 mm pomwe madera aku m'mwera ayembekezere kulandira mvula ya pakati pa 250 mm ndi 300 mm.

Mvula yopitirira mlingo wa 300 mm ikuyembekezeka kudzagwa m'madera a mphepete mwa nyanja monga kwa TA Malanda.


## April 2026




Madera ambiri m'bomali ayembekezere mvula ya mlingo wa pakati pa 100 mm ndi 150 mm mu April.
Pali kuthekera kwakulu koti madera ena amphepete mwa nyanja, kuphatikizapo Nkhatabay boma, TA Mankhamba, ndi kumwera kwa TA Timbiri atha kudzalandira mvura yopitirira 250 mm.
Mvula m'boma la Nkhatabay ikuyembekezeka kufika kumapeto, sabata lomaliza la April, 2026.

Boma la Nkhata bay likuyembekezera kulandira mvula ya mulingo wokhadzika kapena kuposerapo ngakhale pali kuthekera kwakukulu koti m'madera ena mutha kudzagwa mvula yochepera mlingo wokhadzikika mu November komanso February. Mvula yokhazika ikuyembekezeka kugwa kuyambira musabata yachitatu ya December 2025. Mvula m'bomali ikuyembekezeka kufika kumapeto sabata lomaliza la April 2026. Nyengo ya dzija ikuyembekezeka kukhala ya masiku apakati pa 130 ndi 140.
Pali kuthekera kwakulu koti m'madera ena mutha kudzachitika ng'amba mu January komaso February.

| CHINTHECHE | | | |
|---|---|---|---|
| MONTH | NORMAL RANGE | | FORECAST |
| OCT | 1.5 | 9.5 | 8.8 |
| NOV | 41.9 | 96.0 | 42.3 |
| DEC | 160.6 | 233.5 | 220.2 |
| JAN | 188.2 | 259.1 | 163.8 |
| FEB | 175.2 | 224.5 | 149.3 |
| MAR | 249.8 | 446.1 | 406.8 |
| APR | 217.0 | 351.8 | 207.3 |




**Ulosiwu udzaunikidwanso mu mwezi wa December 2025**

For further information contact: The Director of Climate Change and Meteorological Services, P.O. Box 1808,Blantyre.
Tel +265 1 82 47 12 / Cell: +265 882 26 65 79 Email: metdept@metmalawi.gov.mw ; Website: www.metmalawi.gov.mw

Zapangidwa ndi kusindikizidwa ndi thandizo lochokera ku:

© Poster Template by Genigraphics® 1.800.790.4001 www.genigraphics.com